# NSINJIRO ZA CHIYANKHULO

Pomaliza kuwerenga pamutu uno mutha:

- kupereka matanthauzo a nsinjiro zosiyanasiyana za chiyankhulo
- kutsiriza mikuluwiko yomwe ili ndi mipata
- kutsiriza ntchedzero (zifanifani) zomwe zili ndi mipata
- kutsiriza zining’a zomwe zili ndi mipata
- kupereka zitsanzo za mikuluwiko yotsutsana
- kusintha ntchedzero kuti zikhale zining'a
- kusintha mikuluwiko kuti ikhale ntchedzero (zifanifani).

M’mutu uno muphunzira za nsinjiro za chiyankhulo izi: zining'a, mikuluwiko, ntchedzero (zifanifani), miseketso, mizimbayitso, voko ndi nkhambakamwa.

## Kodi nsinjiro za chiyankhulo ndi chiyani?

.M'mawu a m'Chichewa amene amasangalatsa powamva pamene tikulemba kapena kuyankhula amatchedwa nsinjiro za chiyankhulo popeza amakometsa chiyankhulo monganso m’mene nsinjiro zimatha kukometsera ndiwo.

## Kodi chining’a ndi chiyani?

Chining'a ndi mawu amodzi kapena gulu la mawu ochepa onena mozimbayitsa ndipo ali ndi matanthauzo obisika. Anthu akafuna kukambirana nkhani zobisa, kapena zoti anthu ena asadziwe zomwe zikunenedwa; anthuwo amayankhula mophiphiritsa. Zining'a zimakometsa nkhani kotero zimachititsa awerengi kapena omvera kuti amve kukoma kwa chiyankhulo.

**Zitsanzo za zining’a ndi matanthauzo ake**

| **Chining'a** | **Tanthauzo** |
|---|---|
| 1. Bisa nkhope | chita mlubza |
| 2. Byala ufa | mwalira |
| 3. Chitsinzi | munthu wochita zoyipa mobisa |
| 4. Dothi lokhalokha | anthu ambiri |
| 5. Dziko kapena mudzi | manda |
| 6. Dzinthu kapena vinthu | chakudya chambiri |
| 7. Dzuwa | njala |
| 8. Galu wakuda | njala |
| 9. Kalowam'malaya | njala |
| 10.Kabwere mawa | chinthu chosalimba |
| 11.Japani | nsalu yotha msanga |
| 12.Kubisala pachipande | kunama |

| | |
|---|---|
| 13.Kadam'manja | munthu wosawuka |
| 14.Mphemvu m'dyera ku mthiko | munthu wosawuka |
| 15.Kwakwatuke | munthu wosawuka |
| 16.Kamwendo m'njira | munthu woyendayenda |
| 17.Matako akana pansi | munthu woyendayenda |
| 18.Wodya matako a galu | munthu woyendayenda |
| 19.Kaponda chimziri | munthu woyendayenda |
| 20.Kanga ndiwamba | munthu womana |
| 21.Mphungu sataya nthenga | munthu womana kwambiri |
| 22.Kazitape | munthu wodanitsa |
| 23.M'thirakuwiri | munthu wodanitsa |
| 24.Kavuwevuwe | munthu wodanitsa |
| 25.Bwezera phala kum'kobwe | kuchita zolepheretsa nzathu kuti asatichitirenso zabwino |
| 26.Tsinira mafulufute kuuna | kutsekereza zabwino |
| 27.Dula phazi | leka kupita pakhomo la munthu wina |
| 28.Fundika bulangeti | pusitsa |
| 29.Gwira m'maso | pusitsa |
| 30.Phimba m'maso | pusitsa |
| 31.Yala udzu | pusitsa |
| 32.Kumuwaza.mchenga m'maso | kupusitsana |
| 33.Gona pa lumbe | gona osafunda kanthu |
| 34.Igwa nkhope | chita manyazi |
| 35.Thyola bano | kutha msinkhu/kukula/kuchoka pa ubuthu kukhala namwali |
| 36.Gwilitsa fuwa lamoto | kupusitsa munthu/kulindiritsa |
| 37.Kumata phula m'maso | kunamiza mzako |
| 38.Iwala gaga | mwalira |
| 39.Kwatiwa n'kumbuyo komwe | kukwatiwa ndi munthu wolemera |
| 40.Kukwatiwa pantchafu | kukwatiwa ndi munthu wosawuka. |
| 41.Lerera mwana pachinena/pachilolo | kulera momusasatitsa/momupusitsa |
| 42.Kuloza ndege ndi chala | nyada |
| 43.Chotsa chimbenene | chenjeretsa/khaulitsa |
| 44.Nong'oneza bondo | kudandaula utapeza mavuto chifukwa chosamvera |
| 45.Tchera kumwezi | kuzindikira mofulumira za chinyengo cha munthu pamene munthuyo asadachite zomwe anakonzekera zokhudza chinyengocho |
| 46. Thawa mtswatswa wako womwe | dabwa/kukana zomwe unaziyamba |

iwe mwini

47. Tola nkhwangwa ndi mpini womwe   chita mwayi waukulu

## KODI MKULUWIKO NDI CHIYANI?

Mkuluwiko ndi mawu okhala ndi tanthauzo lobisika kapena lophiphiritsa. Timanena mkuluwiko pofuna kubisa tanthauzo la zomwe tikunena kuti ana kapena ena, asadziwe zomwe tikunena. Nthawi zina timanena mkuluwiko pofuna kungokometsa nkhani kukhala ngati nsinjiro zotenderera nkhaniyo kuti ikome. Mkuluwiko nthawi zambiri umakhala chiganizo. Tidziwenso kuti mkuluwiko ndi mutu wa mwambi kapena nkhani kapenanso nthano. Mkuluwiko uliwonse uli ndi nkhani, nthano kapena mwambi wake womwe, tinganene kapena kufotokoza.

## Zitsanzo za mikuluwiko ndi matanthauzo ake

1. Tikonzetikonze adanyula maliro aeni.
   **Tanthauzo:** Munthu usamajijirika pa zinthu za eni chifukwa ukhoza kupezeka pavuto lina lake utalakwitsa china chake.

2. Ulenje umasimba wako.
   **Tanthauzo:** Munthu uzisimba zokhudza iwe osati zokhudza anthu ena.

3. Galu wamkota sakandira pachabe.
   **Tanthauzo:** Wamkulu akamanena kapena kuchita zinthu sangochitapo chabe mopanda kudziwa chomwe akunena kapena kuchita.

4. Kunena kwa ndithendithe nanthambwe adadzitengera.
   **Tanthauzo:** Si bwino kufulumira kuwulula zinsinsi za ena chifukwa kuteroko ukhoza   kupalamula nako.

5. Tsabola wakale sawawa.
   **Tanthauzo:** Zakale zilibe ntchito.

6. Mawu aakulu akoma akagonera.
   **Tanthauzo:** Nzeru za aakulu zimawoneka phindu lake pakapita nthawi.

7. Patsala paja pagona chinziri.
   **Tanthauzo:** Kunena nkhani zakale pofuna kukometsa zinthu pa mlandu.

8. Chetechete sawutsa nyama.
   **Tanthauzo:** Kungokhala chete sikupindula kanthu ngati munthu

akufuna kukwaniritsa chimene akufuna.

9. Ntchenzi idamva mawu oyamba.
**Tanthauzo:** Mawu oyamba ndiwo amene anthu amawerengera kuti ndiwo mawu onena zowona.

10. Kulamula vumbwe n'kulinga uli ndi nkhuku.
**Tanthauzo:** Munthu usamapalamula pamene ulibe populumukira.

11. Tsoka nsinde chimanga chilinda moto.
Tanthauzo: Kuchita tsoka lalikulu.

12. Ili kutali mvula mpesa umera ng'amba.
**Tanthauzo**: Zinthu kumachitika panthawi yake mosatengera kuti wina kapena china chake palibe.

13. Mlendo ndi amene adza n'kalumo kakuthwa.
**Tanthauzo**: Mlendo akhoza kuthandiza pa vuto lomwe eni mudzi angakhale nalo.

14. Mbuto ya kalulu idakula n'tadzawonani.
**Tanthauzo:** Anthu ena amakuza nkhani mowonjezera chabe kapena ponena zabodza.

15. Makale sapanganika, adalira m'thumba la mbala.
**Tanthauzo:** Kamakhalapo kanthu kowululitsa zobisika kapena zachinsinsi

16. Khoswe wapadenga/patsindwi adawululitsa wapadzala.
**Tanthauzo:** Chinthu china chimawululitsa chomwe chinali chobisika.

17. Mthanga kunena adapisa likogwe wa apongozi.
**Tanthauzo:** Tisamalonjeza msanga za chinthu chomwe sitingachikwaniritse.

18. Wakufa sadziwika.
**Tanthauzo:** Wogonja kapena wopambana sadziwika mpaka pothera pake

19. Chifundo chidapha msemamitondo.
**Tanthauzo:** Chifundo nthawi zina chimapweteketsa.

20. Nyama yaliwuma idafa ndi ludzu.
**Tanthauzo:** Liwuma limapweteketsa.

21. Maso aipsa, kamwa likonza.
**Tanthauzo:** Choyipa m'mawonekedwe nthawi zina chimakhala chokoma ukachidya.

22. Nyalugwe chepsa cha mnzake, iye akapha chiwala achita chokoka.
**Tanthauzo:** Pali anthu ena okonda kunyoza za anzawo nthawi zonse koma amakometsa zawo zokha ngakhale zikhale zoyipa.

23. Nyumba ya mwini sawotchera mbewa.
**Tanthauzo:** Osamadalira kwambiri zinthu za eni.

24. Nguluwe idalira msampha utaning'a.
**Tanthauzo:** kuyamba kudandaula vuto litakhala pang'ono kutha.

25. Ukatchula mkango kwera m'mwamba.
**Tanthauzo:** Ukamanena za munthu ndiye kuti munthuyo ali pafupi kufika pamalopo kotero ndi bwino kukonzekera njira yodzipulumutsira nayo iyeyo atakumva zomwe uli kunena za iye.

26. Suzumire adaphetsa mkhalakale.
**Tanthauzo:** Kusaugwira mtima kumadzetsa mavuto.

27. (a) Wamuwonetsa chidameta mduliro nyani.
(b) Wamuwonetsa chidameta nkhanga mpala.
**Tanthauzo:** Wamukhaulitsa

28. Lungalunga mpobadwa chilema chichita kudza.
**Tanthauzo:.** Vuto la pathupi limachita kubwera.

29. Linda madzi apite ndipo uziti ndadala.
**Tanthauzo:** Si bwino kudzitama vuto lisanafike posonyeza kuti latha.

30. Ndawonera momwemu mwambi wa gulugufe.
**Tanthauzo:** Kukhutira ndi zomwe uli nazo.

31. Nkhuyu zodya mwana zidapota akulu.

**Tanthauzo:** Mavuto opalamula ana amavutitsa makolo awo.

32. Kumbire adamka nawo kumanda.
**Tanthauzo:** Si bwino kuzolowera kuchitiridwa chilichonse popeza nthawi ina udzasowa wokuthandiza pamene yemwe amakuthandiza palibe.

33. Wokoma atani wonga fungwe.
**Tanthauzo:** Kudandawulira anthu osayamika ngakhale uwachitire chabwino.

34. Ndim'khulupirira adam'gonetsa m'nkhufi.
**Tanthauzo:** Munthu womudalira nthawi zina ndi amene amakukhumudwitsa kwambiri.

35. Mwana wa pang'ona salephera kuyangala.
**Tanthauzo:** Nthawi zambiri mwana amatengera luso kapena khalidwe kuchokera kwa makolo ake.

36. Tsoka sasimba koma mwayi.
**Tanthauzo:** Ukapulumuka pa tsoka (zovuta) si bwino kuumirira mchitidwe womwe unakuchititsa kuti upezeke mu tsokalo popeza pambuyo pake ukhoza kutaya moyo kapena sungapulumukenso.

37. Papsa tonola, sudziwa mtima wa moto.
**Tanthauzo:** Ukapeza mwayi wochitira zina zake ndi bwino kugwiritsira ntchito mwayiwo.

38. (a) Mamveramvera adachotsa zolo pa ukwati.
(b) Wawona nkhanga mawanga wataya nkhwali.
**Tanthauzo:** Ukamamvera zonena anthu mosaganizira bwino, umataya nazo mwayi womwe unali nawo kale.

39. Mako ndi mako usamuwone kuchepa mwendo.
**Tanthauzo:** Tizipereka ulemu kwa makolo ngakhale akhale onyozeka.

40. Konza kapansi kuti kam'mwamba katsike.
**Tanthauzo:** Munthu ukafuna kuti ena akuchitire zabwino yamba ndiwe kuwachitira zabwino.

41. Choka m'mbuyo khwangwala atole mphutsi.

**Tanthauzo:** Osachita zinthu motsekereza mwayi wa anthu ena.

42. Pita uko si kuyenda.
**Tanthauzo:** Si bwino pamene muli paulendo umodzi kupangana kuti dzera uko chifukwa paulendo wotero kumavuta kukumana kwake.

43. Mbalame zomamwera chigobi chimodzi zimadziwana nthenga.
**Tanthauzo:** Anthu ochita zofanana amayendera limodzi ndi kudziwana kwambiri zochita zawo.

44. (a) Uchembere n'kudyerana.
(b) Kachipande katherere kakoma n'kuyenderana.
(c) Lende (katungwe) n'kukankhana.
(d) Mnzako akakuti konzu, nawe umam'ti konzu
(e) Dombolo n'kuwombolana, nthengu adawombola njiwa.
**Tanthauzo**: Zinthu zimakhala bwino kumathandizana osati m'modzi yekhayekhayo kumathandiza mnzake.

45. Mapanga awiri avumbwitsa.
**Tanthauzo:** Kuchita zinthu ziwiri nthawi imodzi kumapezetsa mavuto kapena kumalepheretsa zinthu kuti zichitike bwino.

46. Taleka n'talawa adatha mphika.
**Tanthauzo**: Munthu akaganiza zoyerekeza kuyamba kuchita chinthu, kumakhala kovuta kudziletsa kuchichita chinthucho chifukwa amafika pochizolowera.

47. Mnzako akapsa ndevu mzimire mawa adzazima zako.
**Tanthauzo:** Mnzathu akakhala pa mavuto tim'thandize popeza mawa lake akhoza kudzatithandiza ife.

48. Akuluakulu ndi m'dambo mozimira moto.
**Tanthauzo:** Akuluakulu ndiwo amathandiza zinthu zikafika povuta.

49. Za kumzinda sawulula.
**Tanthauzo:** Ndi bwino kuti tizisunga chinsinsi cha zimene tawona

kapena tamva.

50. Ukapeza anzako akukazinga maso nawenso tong'ola ako.
**Tanthauzo:** Munthu uzichita nawo zomwe eni mudzi kapena omwe wawapeza akuchita.

51. Sayenda adabala mwana adayenda.
**Tanthauzo:** Usachitire ena choyipa ngakhale iweyo suyenda popeza nthawi ina adzayenda ndi mwana wako ndipo atha kudzamuchitiranso zoyipa anthu omwe aja iweyo udawachitira choyipa.

52. Chinasala chidakanika fisi.
**Tanthauzo:** Munthu akaleka chinthu pamene ali kuchikondabe kapena chomwe adachizolowela kumakhala kovuta kuti achisiye kwathunthu.

53. Ukakhala mwana, mphanje umayambira pamchenga.
**Tanthauzo:** Ukafuna kuphunzira machitidwe a chinthu china ndi bwino kuyamba ndi chosavuta kuchichita.

54. Mulereni ayiwale kwawo.
**Tanthauzo:** Mwana wa munthu wina kapena wamasiye amafunika kumusamala bwino kuti ayiwale kwawo kapena mavuto omwe ali nawo.

55. Tsoka limayambira kumwendo.
**Tanthauzo:** Tsoka limayambira pa kanthu kakang'ono komwe anthu ena sangavomereze kuti kangathe kuyambitsa vuto lalikulu.

56. Zengerezu adalinda kwawukwawu.
**Tanthauzo:** Si bwino kuchita zinthu mozengereza kapena mopanda changu.

57. Ukayipa nkhope dziwa nyimbo.
**Tanthauzo:** Munthu ukazindikira kuti pa chinthu china chake ndiwe wolephera ndi kwabwino kuyesetsa kupeza chinthu chimene ungathe kusonyeza ukatswiri wako.

58. Nkhondo ndi anansi.
**Tanthauzo:** Amakuchitira choyipa nthawi zambiri ndi abale ako

omwe

59. Fisi adakana nsatsi.
**Tanthauzo:** Munthu amakana zomwe akutsimikizira kuti iye sadachite.

60. Msuma sadyera pomwe.
**Tanthauzo:** Ndi bwino pamene wapita kukafufuza chakudya kusiyako osati kumalizira konko chifukwa mwina kumene ungapite utha kudzazifunanso.

61. Nkhwangwa sithwera pa chipala.
**Tanthauzo:** Munthu umadziwitsitsa chinthu ukamachichita kawirikawiri osati nthawi yomwe wangoyamba kuchichita chinthucho.

62. M'mimba ndi m'chipala.
**Tanthauzo:** Ana oberekedwa ndi mayi m’modzi amatha kukhala osiyana m'mawonekedwe, m'makhalidwe ndi m'zochita ngakhale timayembekezera kuti onse angafanane.

63. Chitsime chakale kuphetsa ndi ludzu.
**Tanthauzo:** Si bwino kukhulupirira zakale zokha.

64. Nsangala za pamaliro ngati matenda adakazonda.
**Tanthauzo:** Kujijirika pa zinthu zoti wapeza zothaitha kapena zachitidwa kale pamene poyamba unalibe nazo chidwi

65. Pachedwa msulu pali nyerere.
**Tanthauzo:** Munthu akamachedwa pamene ali ndiye kuti wapeza zomwe zamamusangalatsa.

66. Chibwenzi cha nkhwangwa chokoma pokwera.
**Tanthauzo**: Mchitidwe woyamika chinthu kapena munthu pa nthawi yokhayo pamene ali kukuthandiza koma kenaka n'kumusonyeza kusamulabadiranso chifukwa chakuti iweyo wapeza chithandiza chomwe unkafuna.

67. Akoma akadadza.
**Tanthauzo:** Anthu omwe amakhala abwino poyamba kenaka

amawonetsa makhalidwe oyipa.

68. Malunje sadya sakhwi
**Tanthauzo:** Tisawope tikafuna kuchita chinthu chifukwa cha kuwopsezedwa ndi maonekedwe a chinthucho.

69. Njiwa sasosolera pa nsampha
**Tanthauzo:** Tikafuna kukopa munthu tisamuonetse za chinyengo kapena zomupatsa chikayiko.

70. Watchera kumwezi nkhanga zawona
**Tanthauzo**: Kuchita chinyengo chomwe pambuyo pake chimafika powululika.

71. M'chiwuno mwa mwana simufa nkhuku.
**Tanthauzo:** Mwana ngakhale achite zabwino zotani sayamikiridwa.

72. Tsamba likagwa manyazi agwira mtengo
**Tanthauzo:** Munthu ukachita zopanda pake manyazi amagwira iwe.

73 . Ndikhale nawo adalanda malo
**Tanthauzo:** Kuchita chinthu monyengerera ndi cholinga chopusitsa mwini chinthucho

74. Munthu ndi galu, galu ndi munthu
Tanthauzo: Nthawi zina galu amachita zabwino kusiyana ndi anthu kapenanso zabwino zomwe ndi zofanana ndi zochita za anthu

75. Mlandu sagula ndi chipanda cha mowa
**Tanthauzo:** Si bwino kukometsa wolakwa poweruza mlandu chifukwa chopatsidwa chiphuphu.

76. Ndikadadziwa ndikadaphika therere.
**Tanthauzo:** Tisamadalire zinthu zomwe palibe kapena tikuyembekeza kuti zitheka popeza ukazidalira kwambiri umakhumudwa zikalephera.

77. Mlendo ndi mame.
**Tanthauzo:** Alendo sakhala kuchoka akafika pakhomo.

78. Kupatsa n'kuyikiza.

**Tanthauzo:** Ukamagawirako anthu zinthu zomwe uli nazo nthawi yoti avutika iwo sakuyiwala kotero mwina amadzakuthandiza nthawi yoti nawenso wavutika.

79. Mnzako akapsa ndevu m'zimire.
**Tanthauzo:** Mnzathu tizimuthandiza akakhala pa mavuto chifukwa tsiku lina adzathandiza ife.

80. Nyani samulekera munda.
**Tanthauzo:** Si bwino kusiya kuchita zinthu chifukwa cha munthu wina wowononga kapena wosokoneza zomwe ife tikuchita.

81. Pasambira mfulu kapolo asambira pomwepo.
**Tanthauzo:** Kuchita mwayi chifukwa cha ena omwe mwayi wa chinthu chomwe ukufunacho ali nawo.

82. Kumanga (kutola) khobwe ndi m'mawa.
**Tanthauzo:** Ukafuna kugwira ntchito ndi bwino kugwira ntchitoyo moyambirira kapena mosachedwa.

83. Mwezi satungira mkanda.
**Tanthauzo:** Munthu sagwira bwino ntchito mumdima kotero sibwino kuyembekezera kuchita chinthu pa nthawi imene siyenera kuchitira ntchitoyo.

84. Muyang'ana dzuwa adasochera.
**Tanthauzo:** Ndi bwino kufunsa ngati sitikudziwa.

85. Taya udzu womwetamweta.
Tanthauzo: Taya mwayi wopezapeza.

86. Gona ndi mwini wake wa nyumba.
**Tanthauzo:** Ulamuliro wa chinthu unayenera kuchokera kwa mwini chinthucho.

87. Mwana akalira nyanga ya nsatsi nsemere imufotere yekha.
**Tanthauzo:** Munthu akalimbikira chinthu chopanda phindu ndi bwino kumuleka kuti avutike nacho yekha.

88. Chimanga chilola wopanda mano.
**Tanthauzo**: Zinthu zimapezekera anthu omwe zinthuzo alibe nazo

ntchito.

89. Ukalemera usamayankhulira m'chigulu.
**Tanthauzo:** Ukalemera usamanyadire anzako.

90. Kulemera ndi mchira wa khoswe sukhala kupuluIuka.
**Tanthauzo:**Ulemerero kapena chuma sichikhalira kutha.

91. Ukayendera nzengo usamati asakhwi afumbula.
**Tanthauzo:** Munthu komwe wapita asamayamba kuchita zomwe sichinali cholinga cha ulendo wakewo.

92. Kupulumukira m'kamwa mwa mbuzi.
**Tanthauzo:** Kupulumuka pa mlandu chifukwa chonena bodza lodzipulumutsira nalo.

93. Ziliko n'kulinga utatosako.
**Tanthauzo:** Umboni weniweni ngofunika kuchokera pa zomwe waziwona.

94. Nguluwe idalira msampha utaning'a.
**Tanthauzo:** Kulephera kupirira ndiponso kuda nkhawa kwambiri nthawi yomwe vuto latsala pang'ono kutha.

95. Kulirira kuwutsi.
**Tanthauzo:** Kunamizira zina pamene vuto lilinso lina.

## MIKULUWIKO YOFANANA MATANTHAUZO

Mikuluwiko ina imafanana matanthauzo awo. Onani zitsanzo za mikuluwiko ili m'munsiyi.

1 (a) Apawo ndi mizu ya kachere akumana pansi.
(b) Pamudzi pakakhala pa zitsiru mkamwini asamakulirapo mwendo.
**Tanthauzo:** Ukakhala pamudzi pa eni osamalowerera za pa mtundu kapena kumati ndiwe wanzeru kupambana eni mudzi chifukwa sungadziwe chomwe eni mudzi akupangana.

2. (a) Zengerezu adalinda kwawukwawu.
(b) Muvi woyang'anira suchedwa kugwera m'maso.
(c) Ndapakonda adasiya m'khonde.

(d) Pakadafunda padajiwitsa galu.
(e) Ndiwonetsetse adathetsa nkhosa.
**Tanthauzo:** Kuzengereza pochita zinthu kumapezetsa munthu mavuto.

3. (a) Uchembere n'kudyerana.
(b) Kachipande katherere kakoma n.kuyenderana.
(c) Lende (katungwe) n'kukankhana.
(d) Mnzako akapsa ndevu mzimire mawa adzazima zako.
(e) Mnzako akakuti konzu, nawe umam'ti konzu.
(f) Dombolo n'kuwombolana.
**Tanthauzo**: Mnzako akakuchitira zabwino nawenso ndi bwino kumuchitira zabwino.

4. (a)Kugona pakati n'kuyambirira.
(b) Liwiro la mumchenga n'kuyambira limodzi.
(c) Kayitana kavula ukachedwa upeza katavala.
(d) Kumanga khobwe ndi m'mawa. .
**Tanthauzo:** Pofuna kuchita zinthu ndibwino kuzichita mosachedwa.

5. (a) Mapanga awiri avumbwitsa.
(b)Ichi chakoma ichi chakoma pusi adagwa chagada.
(c) Pawiripawiri sipawuzirika.
(d)Mphuno imodzi siilowa zala ziwiri.
**Tanthauzo:** Si bwino kuchita zinthu ziwiri nthawi imodzi chifukwa nthawi zina umatha kulephera kukwaniritsa zonsezo kapenanso kukwaniritsa chinthu chimodzi chokha mwa zinthu ziwirizo.

6. (a) Anthu ndi miyala sakukutika.
(b) Anthu ndi miyala sawundika.
(c) Anthu ndi mchenga sawundika.
**Tanthauzo:** Anthu alibe kudalirika kapena kupanganika kwenikweni.

7. (a) Awonenji adapha mvuwu m'mono
(b) Awonenji adapha njovu ndi buma.
(c) Njovu idagwa m'mbuna mwa Awonenji.
**Tanthauzo:** Munthu aliyense ali ndi mwayi wake kotero si bwino kuganizira kuti anthu ena wowoneka monyozeka sangapeze mwayi wonga wako.

8. (a) Atambwali sametana awopa kuchekana.
(b) Akapsala sapisana m'thumba.
**Tanthauzo:** Ochenjera okhaokha akadziwana sangathe kuchenjererana chifukwa amaopana.

9. (a) Chalaka nyani nkhuku singatole.
   (b) Chadodometsa mleme chili n'khambi.
   (c) Chati deru chawopsa mlenje.
   (d) Chalaka nyani chili ndi n'khambi.

   **Tanthauzo:** Munthu akasiya chizolowezi chake ndiye kuti chilipo chimene chamudabwitsa kapena chamuchititsa mantha kuti asiye chizolowezicho.

10. (a) Chinasala chidakanika fisi.
   (b) Mtengo umagwera uko udaweramira.
   (c) Madzi sayiwala khwawa.

   **Tanthauzo:** N'kovuta munthu kuleka kapena kusiya chizolowezi chake mosachibwereza.

11. (a) Chisoni chidapha msemamitondo.
   (b) Chisoni chidapha nkhwali.

   **Tanthauzo:** Chisoni chofuna kuthandiza munthu nthawi zina chimapezetse mavuto munthu womvera chisoni mnzakeyo.

12. (a) Chonona chimafumira ku dzira.
   (b) Mbuzi ndi mkota.
   (c) Fodya m'panazale.

   **Tanthauzo:** Ana amatengera mchitidwe wa makolo.

13. (a) Chizolowezi cha namkholowa chidawululitsa mbatata.
   (b) Suzumire adaphetsa mkhalakale.

   **Tanthauzo:** Si bwino kukondana ndi munthu wakhalidwe loyipa chifukwa akhoza kukupezetsa mavuto.

14. (a) Chikondi cha chotsa phazi m'pondepo.
   (b) Chikondi cha bulangeti.

   **Tanthauzo:** Chikondi chodalirika kapena chokondana kuchokera pansi pamtima.

15. (a) Fodya wako ndi uyo ali pa mphuno.
   (b) Kanthu n'kako uvundukula nupenya.

   **Tanthauzo:** Tizidalira zinthu zomwe tili nazo kusiyana ndi zomwe tikungoziganizira.

16. (a) Khoswe wapatsindwi adaulula wapadzala.
   (b) Kanthu nkavumbu kadavurnbulaa mende pachisa.

   **Tanthauzo:** Chinthu china chimatha kuwululitsa chinthu chinzake

chomwe chinali chobisika.

17. (a) Kwa eni kudyetsa nthanga dzungu nulifuna.
(b) Kwa eni kusunsitsa msuzi ndiwo nuyifuna
**Tanthauzo**: Munthu ukakhala kwa eni ulibe ulamuliro kapena mphamvu zochitira china chake ndipo umalephera kuchita zomwe ukadachita ukadakhala kwanu.

18. (a) Khwangwala warnantha adafa ndi ukalamba.
(b) Phukusi la moyo sakusungira ndi mnzako.
**Tanthauzo:** Munthu wamantha amakhala zaka zambiri asanafe chifukwa manthawo amamuthandiza kuti asamachite mphulupulu zomwe zingamuchititse kuti afe msanga

19. (a) Kutsutsa galu n'kukumba.
(b) Ziliko n'kulinga utatosako.
**Tanthauzo:** Sibwino kutsimikizira chinthu usadapeze umboni weniweni

20. (a) Kukhala awiri si mantha.
(b) Ichi n'chiyani n'kulinga muli awiri.
**Tanthauzo**: Anthu akakhala awiri amatha kuchita zinthu modalirana ndipo amatha kuthandizana wina akapezeka pa mavuto.

21. (a) Linda madzi apite ndipo uziti ndadala.
(b) Mthanga kunena adapisa likongwe wa apongozi.
(c) Kunena kwa ndithendithe nanthambwe adadzitengera.
**Tanthauzo**: Sibwino munthu kudzitama kapena kulonjez.eratu chinthu zotsatira zake zisanadziwike kwenikweni chifukwa mwina zotsatira zake zitha kukuika m'mavuto kapena kukutsutsa.

22. (a) Likawoniba wotheratu.
(b) Papsa tonola sudziwa mtima wa moto.
**Tanthauzo:** Si bwino kuchita zinthu mochedwa mwayi ukapezeka.

23. (a) Lero lomwe lidadetsa mnthengu.
(b) Tsiku limodzi siliwoza mbewa.
**Tanthauzo:** Nthawi zina ndi bwino kulolera kuti tizidikira pochita zirithu chifukwa tikachita mofulumira nthawi zina zinthuzo sizichitika bwino.

24. (a) Mwana mnyanja alimbikira mpani wake.
(b) Pagule fumbi ndiwe mwini.
(c) Mpani wa mbewa utsatira mwini.

**Tanthauzo:** Munthu aliyense amalimbikira kuchita zinthu zake kuti ndizo zichitike bwino kwambiri kusiyana ndi kulimbikira zinthu za ena.

25. (a) Nkhuyu zodya mwana zidapota akulu.
    (b) Akuluakulu ndi m'dambo mozimira moto.
    **Tanthauzo:** Nthawi zambiri ana akapalamula, vuto lonse limafikira kwa makolo ndipo ndiwo amavutika nalo.

26. (a) Mwini phale sakuda chala.
    (b) Chala sichiloza mwini.
    **Tanthauzo:** Ndi chinthu chovuta kuti munthu adziwone kuyipa kwa iye mwini.

27. (a) Mbalame ikatera pauta silasika.
    (b) Khoswe akakhala pa mkhate sapheka.
    **Tanthauzo:** Kumakhala kovuta kuti uweruze mlandu wam'bale wako makamaka atapezeka kuti ndi woyenera kupatsidwa chilango.

28. (a) Mawu akulu akoma akagonera.
    (b) Tinkanena adathira msiizi.
    **Tanthauzo:** Mawu akulu amakumbukiridwa pakapita nthawi ndiponso pamene zomwe amanenazo zachitikadi.

29. (a) Mutu umodzi susenza denga.
    (b) Chala chimodzi sichiswa nsabwe.
    (c) Kalikokha n'kanyama; tili tiwiri n'tiwanthu.
    **Tanthauzo:** Palibe munthu yemwe angathe kuchita zinthu zonse payekha kotero ndibwino kumathandizana kapena kumadalirana.

30. (a) Mwachaje satafuna.
    (b) Ndawonera momwemu mwambi wa gulugufe.
    **Tanthauzo:** Ndi bwino munthu kukhutitsidwa ndi zinthu zomwe uli nazo ngakhale zili zochepa.

31. (a) Madoli (matodwe) adafera mchenga woyera.
    (b) Chikomekome chankhuyu m'kati muli nyerere.
    (c) Kuyera ndi madzi a nyemba.

(d) Maso apatali amawongola mtengo.
(e) Mawonekedwe apusitsa.

**Tanthauzo:** Zinthu zina zimangokongola m'mawonekedwe chabe pomwe sizili zokongola kwenikweni.

32. (a) M'mphechepeche mwa njovu sapitamo kawiri.
(b) Chibwereza chidaphetsa kunda.
(c) Bza sapita kawiri.

**Tanthauzo:** Ngati munthu wapulumuka pa vuto mwamwayi si bwino kubwereza kuchita chinthucho.

33. (a) Mawu m'poyamba otsiriza ndi mang'ombe.
(b) Ntchenzi idamva mawu oyamba.

**Tanthauzo:** Ndi bwino munthu kusamala mawu oyamba omwe ukufuna kuyankhula chifukwa ndiwo mawu omwe anthu omvetsera amawerengera kuti ndiwo amene iwe wanena.

34. Mvula ikakuwona litsiro siikata

**Tanthauzo:** Nthawi zina mavuto akayamba kukuchitikira amakuchitikira mowirikiza.

35. (a) Ndapakonda adasiya m'khonde.
(b) Muvi woyang'anira suchedwa kugwera m'maso.
(c) Pakadafunda padajiwitsa galu.
(d) Zengerezu adalinda kwawu kwawu.
(e) Ndiwonetsetse adathetsa nkhosa.

**Tanthauzo**: Kuzengereza pochita chinthu kumagwetsa munthu m'mavuto.

36. (a) Nguwo yobwereka silimba m'thupi.
(b) Nyumba ya mwini sawotchera mbewa.
(c ) Nkhunzi yobwereka samangira khola.

**Tanthauzo:** Si bwino kudalira chinthu chobwereka chifukwa mwini wake atha kuchifuna nthawi ina iliyonse.

37. (a) Njiwa sasosolera pa msampha.
(b) Watchera ku mwezi.

**Tanthauzo:** Munthu akamachita zachinyengo ndi anzake nthawi imafika yoti anzakewo amamutulukira za chinyengozo.

38. (a) Nkhwangwa yobwereka sikhala kuguluka.
(b)Nkhwangwa yobwereka sikhala kusweka mpini.

**Tanthauzo:** Chinthu chobwereka, munthu sachedwa kuchita nacho ngozi.

39. (a) Nzeru n'zayekha adaviika nsima m'madzi.
(b) Safunsa adadya phula.
(c) Kandimverere adamva za m'maluwa.
(d) M'yang'ana dzuwa adasokera.

**Tanthauzo**: Ngati tikukayika kapena sitikudziwa zoyenera kuchita ndi bwino kufunsa kuti tichite zinthu moyenera kapena mosalakwitsa.

40. (a) Msonkhamsonkha adang'amba thumba.
(b)Tsokonombwe adatha dziko n'kudumpha.

**Tanthauzo:** Nthawi zina ndi bwino kuchita zinthu mosathamangitsa ndi bwinonso kulimbikira kufikira zochita kapena zomwe ufuna zitatheka.

41. (a) Ukapanda mano usamaswe phale.
(b) Ukapanda chala usamadane n'kuloza.
(c) Ukasawuka usamagwire nyanga.

**Tanthauzo**: Ngati sungathe kugwiritsa ntchito chinthu usamadane ndi amene angathe.

42. Chili ku mnzako n'kumati chigwire nyanga.

**Tanthauzo**: Munthu amawona vuto la mnzake ngati si vuto ayi koma vuto ngati lomwelo likamuwonekera ndi pamene amaliwona kuti ndi vutodi.

43. Ali dere n'kulinga utayenda naye.

**Tanthauzo**: Chinthu chilichonse chili ndi zovuta zake kotero ndi bwino kuti munthu asasiye kuchita chinthu chomwe akufuna chifukwa cha zovuta zina za chinthucho.

44. (a) Wakwatira kwa mphenzi sawopa kung'anima.
(b) Walira mvula walira matope.

**Tanthauzo**: Chinthu chilichonse chili ndi zovuta zake kotero ndi bwino munthu asasiye chinthu chomwe akufuna chifukwa cha zovuta zina chinthucho.

45. (a) Wakwatira mende waleka chitute.
(b) Wawona nkhanga mawanga wataya nkhwali.

**Tanthauzo**: Si bwino kutengeka ndi zinthu chifukwa cha mawonekedwe chabe koma ndi bwino kuwonetsetsa ubwino wake kapena kuyipa kwake chinthucho chifukwa mwina utha kutaya mwayi wopezapeza.

46. (a) Umanena chatsitsa dzaye kuti njovu ithyoke mnyanga.
(b) Chulukechuluke ngwa njuchi umanena imene yakuluma.
**Tanthauzo**: Munthu uzinena chenicheni chomwe chayambitsa kuti vutolo lichitike.

47. (a) Wokawona nyanja adakawona ndi mvuwu yomwe.
(b) Ukayenda m'tchire wayendera zonse.
**Tanthauzo**: Nthawi zambiri ukayendera zina umatha kuchita mwayi wochitiranso zina zake.

48. (a) Zachoka ndundu tiyanikeko inswa.
(b) Paunyinji sabudulirapo.
**Tanthauzo**: Anthu ena omwe safuna kuti anzawo ena amveko zachinsinsi zawo iwo ayesetsa kuti akambirane zachinsinsizo ena aja akachokapo, kapena amapita pamalo ena poduka mphepo.

49 (a) Woluka nsengwa adyera m'chipapa.
(b) Wosoka mphasa agonera pa zidutswa.
(c) Wowumba mbiya aphikira m'phale.
**Tanthauzo:** Nthawi zina munthu wogwira ntchito zaluso sakonda kutengako chimodzi mwa zinthu zomwe iyeyo amapanga mwina chifukwa choganiza kuti akatero akuwononga. Iye amagwiritsa ntchito zipangizo zakutha kapena zosweka.

## MIKULUWIKO YOTSUTSANA M'MATANTHAUZO

Pali mikuluwiko ina yomwe imatsutsana matanthauzo. Zitsanzo za mikuluwiko yotere ndi izi:

1. (a) Chibwereza chidaphetsa kunda.
(b) Bza sapita kawiri.
(c) M'mphechepeche mwa njovu sapitamo kawiri.
**Wotsutsa**: Mphini zobwereza n'zomwe zimatumba.

2. Kanthu n'kako uvundukula nupenya.
**Wotsutsa:** Zathu salowa m'khola.

3. Kuchulukana n'kwabwino kuipira kuthetsa mchere.

**Yotsutsa:** (a) Kali kokha n'kanyama, tili tiwiri n'tiwanthu.
(b) Njuchi zikachuluka siziika uchi.

4. Kuwona maso a nkhono n'kudekha.
**Yotsutsa:** (a) Ndiwonetsetse adathetsa nkhosa.
(b) Zengerezu adalinda kwawukwawu.
(c) Muvi woyang'anira suchedwa kulowa m'maso.
(d) Ndapakonda adasiya m'khonde.
(e) Pakadafunda padajiwitsa galu.

5. (a) Mawu aakulu akoma akagonera.
(b) Tinkanena anathera m'siizi.
**Wotsutsa:** Tsabola wakale sawawa.

6. Mwala wogubuduzika sumera ndere.
**Yotsutsa**: (a) Pamodzipamodzi padawoletsa dzungu.
(b) Mwana wa ng'ona sakulira dziwe limodzi.

7. (a) Ukayenda m'tchire wayendera zonse.
(b) Wokawona nyanja adakawona ndi mvuwu yomwe.
**Wotsutsa**: Ukayendera nzengo usamati asakhwi afumbula.

## MAWU ENA OKOMETSA NAWO CHIYANKHULO

### 1. Ntchedzero

Ntchedzero ndi mawu omwe matanthauzo ake ndi oserewula mwina oseketsa. Palinso ntchedzero zina zomwe matanthauzo ake ndi okwiyitsa kapena opsetsa mtima. Ponena ntchedzero anthu amafananitsa munthu ndi chinthu china chake pogwiritsa ntchito mawu woti '*ngati*' kapena '*monga*'. Izi zikusonyeza kuti ndi kofunika kuzindikira kuti ntchedzero ndi mtundu wa zifanifani.

**Zitsanzo:**

| *Ntchedzero* | *Tanthauzo* |
|---|---|
| a. timawu ngati mngoli | - mawu okongola zedi poyimba kapena poyankhula |
| b. kuwala ngati nyenyezi | - mawonekedwe osagalatsa |
| c. kutsekemera monga uchi | - kuzuna kwambiri kwa chinthu |
| d. kuwawa ngati ndulu ya ng'ona | - kuwawa kwambiri kwa zakudya kapena |

zakumwa

e. kuswana ngati dzombe - kuchulukana kwambiri kwa zinthu
f. chifundo monga cha msemamitondo - kukhala ndi chifundo chachikulu chopezetsa mavuto munthu womverera chifundo mnzakeyo

## 2 Ntchedzero zachilengo

Ntchedzero ya chilengo ndi mawu ochedzera munthu kapena chinthu monyoza. Mawuwa amapsetsa mtima mpaka mwina anthu akhoza kumenyana kapena kukwiyirana chifukwa chonenana chilema kapena mawonekedwe oyipa a wina ndi mnzake. Zilengo nazonso ndi mtundu wa zifanifani popeza zimasonyeza kufananitsa zinthu.

**Zitsanzo:**

| *Chilengo* | *Tanthauzo* |
|---|---|
| a. Chimutu kukula ngati mdenga | - mutu waukulu kwambiri |
| b. Kuda ngati makala | - kuda kwambiri |
| c. Kuda monga kuseri kwa m'phika | - kuda kwambiri |
| d. Kuda monga chikuni chowawuka ndi moto | - kuda kwambiri |
| e. Mawu ngati chule | - mawu oyipa makamaka poyimba |
| f. Mphuno ngati chikololo cha azungu | - mphuno yaitali |

## Kusintha ntchedzero/zifanifani kukhala zining'a

Kumatheka kusintha ntchedzero/chifanifani kuti zikhale zining'a makamaka pamene tikufanizira chinthu china ndi chinzake. Kufaniziraku kukhoza kuchitika moganizira mawonekedwe, machitidwe, mamvekedwe kapena makhalidwe a zinthu zomwe tikukambira nkhani.

**Zitsanzo:**

| | *Mawu mawu othandiza* | *Ntchedzero (Chifanifani)* | *Chining'a (ndi othandizira)* |
|---|---|---|---|
| i. | Ndiwe | wokongola ngati nyenyezi | ndiwe nyenyezi |
| ii. | Ndiwe | wochenjera ngati kalulu | ndiwe kalulu |
| iii. | Ndiwe | wakuda ngati mtsiro | ndiwe mtsiro |
| iv. | Ndiwe | wonunkha ngati kanyimbi | ndiwe kanyimbi |
| v. | Ndiwe | wopusa ngati mbuzi | ndiwe mbuzi |
| vi. | Ndiwe | womveka kwambiri ngati ng'oma | ndiwe n'goma |
| vii. | Ndiwe | wabodza ngati mthirakuwiri | ndiwe nthirakuwiri |
| viii. | Ndiwe | wamantha ngati fisi | ndiwe fisi |
| ix. | Ndiwe | wokonda kukhala m'nyumba ngati thunga | ndiwe |

| | | |
|---|---|---|
| | | thunga |
| x. Ndiwe | wosadziwa kusambira ngati mbiya | ndiwe mbiya |

## KUSINTHA MIKULUWIKO KUKHALA NTCHEDZERO (ZIFANIFANI)

Kumatheka kusintha mikuluwiko kuti ikhale ntchedzero (zifanifani) kapena kupanga ntchedzero (zifanifani) kuchokera ku mikuluwiko.

**Zitsanzo:**

| *Mkuluwiko* | *Ntchedzero* |
|---|---|
| 1. Fisi akagwa m'mbuna sayankhula kanthu | Kusayankhula ngati fisi wogwa m'mbuna. |
| 2. Chala sichiloza mwini. | Kusaloza mwini ngati chala. |
| 3. Tsabola wakale sawawa. | Kusawawa ngati tsabola wakale. |
| 4. Kuzingwa kwa kalulu kukapsa. | Kuzingwa monga kalulu kukapsa. |
| 5. Ntchenzi idamva mawu oyamba. | Kumva mawu oyamba ngati ntchenzi. |
| 6. Ukakhala wopanda chala usamadana n'kuloza. | Kudana n'kuloza monga wopanda chala. |
| 7. Mwana wa n'gona sakulira dziwe limodzi. | Kusakulira pamodzi ngati mwana wa ng'ona. |
| 8. M'mphechepeche mwa njovu sapitamo kawiri | Kusapitamo kawiri ngati m'mphechepeche mwa njovu |
| 9. Khoswe akakhala pa mkhate sapheka. | Kusapheka monga khoswe akakhala pa mkhate |
| 10. Mbalame ikatera pa uta silasika. | Kusalasika ngati mbalame yotera pa uta. |

## NSEKETSO

Miseketso imakhala ndi mawu ofanana kalembedwe kapena katchulidwe kokha. Munthu wakumva nseketso akapanda kuzindikira cholinga cha munthu woyankhulayo kapena wolembayo, wakumvayo kapena wowerengayo, akhoza kukhala ndi tanthauzo lina. Pambuyo pake munthuyo akazindikira zomwe winayo akutanthauza zimaseketsa. Miseketso imakhala ngati ili ndi tanthauzo limodzi pamene imakhala ndi matanthauzo angapo.

*Zitsanzo*:

1. Ndimayikanyanga m'nyumbamu.

**Tanthauzo:** (a) Ndimadya nsima m'nyumbamu.
(b) Ndimayika mankhwala aufiti m'nyumbamu.

2. Kholowa m'kabudula amamera?

**Tanthauzo:** (a) Kodi kholowa mukamudula amamera?
(b) Kodi kholowa m'kati mwa kabudula amamera?

3. Kodi zimathamanga ng'ombezo m'kasaka?

**Tanthauzo:** (a) Kodi ng'ombe zimathamanga m'kazisaka?
(b) Kodi ng'ombe zimathamanga m'saka?

4. Kodi ufa ukadya?

**Tanthauzo:** (a) Kodi umwalira ukadya?
(b) Kodi ufa wachimangawu ukadya?

5. Kodi nkhuku m'katsekera zimatuluka?

**Tanthauzo:** (a) Kodi nkhuku zikakhala monga m'khola ndi kutseka kukhomo kwa kholalo, nkhukuzo zimatuluka?
(b) Kodi nkhuku zikakhala mu tsekera zimatuluka?

6. Kodi zaka zako ndi zaka zanga n'zofanana?

**Tanthauzo:** (a) Kodi za akazi ako ndi akazi anga ndi zofanana?
(b) Kodi zaka zako ndi zaka zanga n'zofanana?

7. T'ikumana kukachaso.

**Tanthauzo:** (a) Tikumana ku kacha m'mawa.
(b) Tikumana ku malo omwera mowa wa kachasu.

## MIZIMBAYITSO

Mzimbayitso ndi mawu onena nkhani mopanda chindunji; kapena tinene kuti mophiphiritsa. Mizimbayitso ilipo yosiyanasiyana ndipo ina mwa iyo ndi iyi:

(a) **Mizimbayitso yonyoza**

Iyi ndi mizimbayitso ya matanthauzo onyoza. Poyankhula munthu amachita ngati akuyamikira, pomwe m'maganizo ake muli kunyogodola kapena kuyipitsa.

**Zitsanzo:**

| *Mizimbayitso* | *Tanthauzo* |
|---|---|
| Chisotichi chakukhala bwino | - kuyamikira monama pamene munthuyo chisoticho sichidamukhale bwino |
| Koma ndiye ndiwozi wazikazinga bwino kwambiri | - kuyamikira monama pamene ndiwozo sadakazinge bwino |

(b) **Mizimbayitso yonyalapsa**

Mawu onyalapsa amanenedwa ndi cholinga chopereka ulemu kapena kuchepetsa nthumanzi kapenanso mantha omwe munthu ali nawo: Munthu amanena mwaulemu kapena mosafuna kutchula mawu omwe akhoza kusonyeza ngati mawu achipongwe kapena opanda ulemu kapena otukwana kapenanso ochititsa phuma.

**Zitsanzo:**

| | *Mizimbayitso yonyalapsa* | *Tanthauzo* |
|---|---|---|
| i. | Abambo aja atisiya | - Abambo amwalira |
| ii. | Mwana wapambuka | - Mwana wanyera kapena wasoma. |
| iii. | Mwana wayipitsira pano | - Mwana wanyera kapena wasoma. |
| iv. | Ndifuna ndikataye madzi | - Ndifuna ndikakodze. |
| v. | Ndinapita kukayimirira | - Ndinakakodza. |
| vi. | Nambewe ngodwala mwana. | - Nambewe akuyembekezera kubala |
| vii. | Mkaziyu ngoyendayenda kapena wadama. | - Mkaziyu ndi wachiwerewere, hule |
| viii. | Mnyamata chamuyambwa chitedze | – Mnyamata watenga nthenda chifukwa cha chiwerewere. |
| ix. | Mayiyu wapita padera | - Mayiyu wabala mwana wakufa. |
| x. | Mtsikanayu ali ndi pakati | - Mtsikanayu ali ndi mimba. |

## VOKO

Voko ndi mawu onena mowonjezera kapena mosinjirira chabe pamene zonenedwazo sizili choncho kwenikweni ayi.

**Zitsanzo:**

a) Ku ukwatiko kudalibe ndi munthu yemwe.
(Akunena izi pamene anthu angapo adaliko ku ukwatiko.)
b) Kuli chimunthu chamnanu kumsonkhanoko.
(Akunena izi pamene kuli anthu owerengeka chabe.)
c) Mwana wanga kusukulu dzina n'1ake lokha

(Akunena izi pomwe mwanayo sadachite kutchuka kwenikweni kusukuluko)

d) Panalibenso wina woyimba bwino ndine ndekha.

(Akunena izi pomwe ena oyimba bwino kuposa iye analiko)

e) M'dengu muli gwa mopanda ndi ufa womwe.

(Akunena izi pamene ufa ulimo pang'ono woti n'kukwanira kuphikira nsima yochepa)

f) Zovala zonse zijatu n'zogula ine.

(Akunena izi pomwe iye adagula chovala chimodzi kapena ziwiri zokha)

## NKHAMBAKAMWA

Nkhambakamwa ndi nkhani yongonena zinthu mocheza chabe kapenanso zopanda nazo umboni, ndipo mwina sizingachitikenso choncho ngakhale zikuyankhulidwa. Nthawi zina munthu amayankhula zakale ngakhale kalero sizidali choncho kwenikweni kumbali yake. Munthu amangoyankhula pofuna kusonyeza kuti sadali umo alili tsopano. Mawu ena amanena pongofuna kuwopseza kapena kuwonjezera kapenanso kukometsa chabe.

***Zitsanzo:***

a) Ana inu, tidali atsikana ife kale.

(kutanthauza kuti anali okongola, pomwe mwina sadali wotero)

b) Ndidali munthu ine masiku amenewo.

(kutanthauza kuti adali wowoneka bwino kapena wachuma pomwe mwina adalibe chilichonse)

c) Ndimkati ndikamenya munthu kuferatu.

(kutanthauza kuti adali ndi mphamvu zambiri pamene mwina sadali choncho)

d) Sunganditero ine! Uwona.

(kutanthauza kuti ndi wowopsa kapena wosati n'kusewera naye pamene mwina sali choncho)

e) Tinkamenyatu ife, tili anyamata.

(kutanthauza kuti adali ndi mphamvu zambiri pamene mwina adalibe mphamvu zambiri)

### Ntchito

Perekani matanthauzo a zining'a izi:

(a) moyo wamphale

(b) nsalu yalekaleka

(c) gona palumbe

(d) wapsa katope

Tsirizani mikuluwiko iyi:

(a) Ukayendera nzengo usamati asakhwi________________

(b) Kwa eni kudyetsa nthanga dzungu_____________

(c) Likawomba_____________

(d) Nyalugwe chepsa ka mnzake koma iye akapha chiwala achita____
___________